## PHUNZIRO LA 31

1. Kodi Mulungu ankavatsogolera a Ejipito kupita ku dziko lanji?
-Mulungu ankavatsogolera a Isirayeli kubwelera ku dziko la kanani.

2. Kodi Mulungu ankavatsogolera bwanji a Isirayeli masana?
-Masana, Mulungu ankavatsogolera a Isirayeli ndi mtambo.

3. Kodi Mulungu ankavatsogolera bwanji a Isirayeli usiku?
-Usiku, Mulungu ankavatsogolera a Isirayeli ndi chipilara cha moto.

4. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anavatsogolera a Isirayeli mpaka m'mbali mwa Nyanja yofiira?
-Mulungu ankafuna kuti avawonetse a Isirayeli ndi a Ejipito kuti IYE ndi Mulungu m'modzi yekha.

5. Kodi a Isirayeli anachita chiyani atamuwona Farawo ndi asilikali ake akubwera kudzavagwiranso?
-A Isirayeli ankamunena Mose kuti bolani anakatsalirabe ku Ejipito.

6. Kodi a Isirayeli anakatha kudzipulumutsa okha?
-Iyayi.

7. Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli sanakatha kudzipulumutsa okha?
-Nyanja Yofiira inali kutsogolo kwawo, mapili anali ku mbali zonse za iwo, ndipo Farawo ndi asilikali ake anali kumbuyo kwawo.

8. Kodi yekha amene anakatha kuvapulumutsa a Isirayeli anali ndani?

-Mulungu.

9 Kodi chifukwa chiyani kunali kosavuta kwa Mulungu kutsagula Nyanja yofiira?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anayilenga Nyanja yifiirayo.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi oyang'anira Nyanja zonse.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wa mphamvu kwambiri, ndipo akhoza kuchita china chilichonse.

10. Chifukwa chakuti Farawo ndi asilikali ake ankabwera kudzavagwiranso a Isirayeli, kodi Mulungu anachita chiyani pofuna kuvapulumutsa a Isirayeli?
-Mulungu anayika mtambo pakati pa a Isirayeli ndi Farawo pamodzi ndi asilikali ake.
-Mtambowo umkawala ku mbali imene a Isirayeli anali ndipo unkapangitsa mdima ku mbali imene Farawo pamodzi ndi asilikali ake anali.

11. Kodi Mulungu anachita chiyani, Farawo pamodzi ndi asilikali ake atavatsatira a Isirayeli mpaka Mnyanja yofiira ija?
-Mulungu anamumiza Farawo pamodzi ndi asilikali ake mnyanja yofiira ija.

12. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anavateteza a Isirayeli kuti asafe?
-Mulungu anavateteza a Isirayeli chifukwa chakuti IYE analonjeza zotumiza Mpulumutsi kupitira mwa Aburahamu, ndi a Isirayeli.
-Mulungu anavatetezanso a Isirayeli chifukwa chakuti Iye ankafunanso kuti adzatumize Mawu AKE, Bayibulo, kwa anthu onse kupitira mwa Aburahamu ndi a Isirayeli.

-Mulungu atamuwononga Farawo ndi asilikali ake Mnyanja Yifiira ija, kodi Iye amkavatsogolera a Isirayeli kupita kuti?



anavapatsa a Isirayeli madzi.

-Tikamumvera Mulungu, Mulungu adzatipulumutsa ife.
-Tikapanda kumumvera Mulungu, Mulungu sadzatipulumutsa ife.

-Tiyenera kumumvera Mulungu potsata njira Yake.
-Sitingathe kumumvera Mulungu potsata njira yathu.

-Ngati titsate njira yathu, Mulungu sadzatipulumutsa ife.
-Mulungu adzatipulumutsa ife tikangotsata njira Yake yokha.

-Mulungu yekha ndi amene angathe kutipulumutsa ife ku mphamvu ya uchimo.
-Mulungu yekha ndi amene angathe kutipulumutsa ife ku mphamvu ya imfa.
-Mulungu yekha ndi amene angathe kutipulumutsa ife ku mphamvu Satana.

-Kodi Mulungu anavapulumutsa a Isirayeli malingana ndi njira imene iwowo anasamkha?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anavapulumutsa bwanji a Isirayeli?
-Malingana ndi njira imene Mulunguyo anasankha.

-Kodi Mulungu amavapulumutsa bwanji anthu onse?
-Malingana ndi njira imene Mulungu amasankha.

5-Chomcho AMBUYE anamuwuza Mose kuti, “Upite kumene kuli anthuwo, ndipo utsagane ndi akuluakulu ena a a Isirayeli, ndipo mukayime patsogolo pa anthuwo. Ndipo ukatenge ndodo imene unakanthila madzi a mu mtsinje wa Nayilo ija.

6-Kumeneko Ine ndikayima patsogolo pako, pa tanthwe limene lili pa phiri la Holebu. Ukakanthe tanthwelo ndipo madzi akatuluka mu tanthwelo kuti anthuwo akamwe.”

-Kodi Mulungu anamuwuza Mose kuti achite chiyani kuti apeze madzi?
-Mulungu anamulamula mose kuti akanthe tanthwe ndi ndodo yake kuti madzi atuluke.

-Mose anakamvera Mulungu, Mulungu anakavapatsa a Isirayeli madzi kuchokera mu tanthwe.

-Kodi ndi ndani yekha amene anakatha kuvapatsa a Isirayeli madzi kuchokera mu tanthwe?
-Mulungu.

-Kodi Mose anamumvera Mulungu?

Tiyeni tiverenge Ekisodo 17:6b

6-Chomcho Mose anachita zimenezi pa maso pa a akuluakulu a a Isirayeli.

-Mose anamumvera Mulungu.

-Mose anakantha tanthwe ndi ndodo yake ngati m’mene Mulungu anamuwuzira.

-Chifukwa chakuti Mose anamumvera Mulungu, Mulungu



-Ku chipululu.

-Kodi chipululu ndi chiyani?
-Chipululu ndi ku malo kumene kuli mchenga wambiri.
-Kulibe mitengo ku chipululu.
-Kulibe udzu ku chipululu.
-Kulibe mchenga ku chipululu.

-Ku chipululu kumakhala mchenga okhaokha.

-Mulungu akuvatsogolera a Isirayeli mchipululu muja, kodi a Isirayeli anachita chiyani?

Tiyeni tiverenge Ekisodo 16 :1-3

1-Khamu lonse la a Isirayeli, linachoka ku Elimu, pa tsiku la 15 mwezi wachiviri chichokele ku Eguputo, anafika ku chipululu cha Sini, chimene chili pakati pa Elimu ndi Si-nayi.

2-Ndipo khamu lonse la a Isirayeli linamudandawuli-ra Mose ndi Aloni mchipululu muja kuti,

3-“Zinakakhala bwino AMBUYE anakatipha ife ku Eguputo konkuja, Kumene tinkakhala tikudya nyama ndi mikate, ndipo tinkakhuta. Koma inu mwatitenga ife mpaka ku chipululu kuno kuti mutiphe ndi njala.”

-A Isirayeli amkamunena Mose ndi Aloni.
-Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli amkamunena Mose ndi Aloni?
-Chifukwa chakuti analibe chakudya.

-Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli analibe chakudya?
-Chifukwa chakuti mchipululu munalibe chakudya.

-Mchipululu munali mchenga okhawokha.

-Kodi Mose anakatha kwafunila a Isirayeli chakudya mchipululu muja?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti mchipululumo munalibe chakudya.

-Kodi a Isirayeli anakatha kudzifunila okha chakudya mchipulu muja?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti mchipululumo munalibe chakudya.

-Kodi ndi ndani yekha amene anakatha kuwapatsa a Isirayeli chakudya mchipululu muja?
-Mulungu.

-Kodi a Isirayeli anakhulupilira mwa Mulungu kuti avapatsa chakudya mchipululu muja?
-Iyayi.

-M'malo mokhulupilira mwa Mulungu kuti avapatsa chakudya mchipululu muja, kodi a Isirayeli anachita chiyani?
-Amkamunena Mose ndi Aloni.

-Kodi Mulungu anavamva a Isirayeli pamene amkamunena Mose ndi Aloni?
-Inde.

-Kodi Mulungu anamuwuza chiyani Mose?

Tiyeni tiverenge Ekisodo 16:11-12

11-AMBUYE anamuwuza Mose kuti,



-Kodi Mose anakatha kuwafunira madzi a Isirayeli mchipululu muja?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti mchipululu muja munalibe madzi.

-Kodi a Isirayeli anakatha kudzifunira okha madzi mchipululu muja?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti mchipululu muja munalibe madzi.

-Kodi ndi ndani yekha amene anakatha kuvapatsa a Isirayeli madzi mchipululu muja?
-Mulungu.

-Kodi a Isirayeli anamukhulupilira Mulungu kuti Iye avapatsa madzi mchipululu muja?
-Iyayi.

-M'malo momukhulupilira Mulungu kuti avapatsa iwo madzi mchipululu muja, kodi a Isirayeli anachita chiyani?
-A Isirayeli ankamunena Mose ndi Aloni.

-Kodi Mulungu ankavamva a Isirayeli pa nthavi imene iwo ankamunena Mose ndi Aloni?
-Inde.

-Kodi Mulungu anavasiya a Isirayeli kuti afe ndi ludzu?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anamuwuza chiyani Mose?

Tiyeni tiverenge Ekisodo 17:5-6a

-Mulungu sanayivale kwapatsa a Isirayeli mana ngakhale tsiku limodzi

-Mulungu amasunga malonjezo ake.

-Ngakhale kuti Mulungu ankavapatsa a Isirayeli zimziri ndi mana, a Isirayeli ankadandawulabe.

Tiyeni tiverenge Ekisodo 17:1-4

1-Khamu lonse la a Isirayeli linachoka ku chipululu cha Sini, ndipo ankayenda monga m'mene AMBUYE ankavalamulilira, kuchoka pa malo a chigono china kupita pa malo a chigono china. Ndipo anamanga masakasa awo ku Refidimu. Kumeneko kunalibe madzi akumwa anthu.
2-Pamenepo anthuwo anayamba kutsutsana naye Mose, nati, "Tipatseni madzi timwe." Koma Mose anafunsa kuti, " Kodi chifukwa chiyani mukutsutsana ndi ine? Muvayeseranji AMBUYE?"
3-Koma anthu aja anamva ludzu kwambiri, ndipo anthuwo anamudandawulira Mose kuti, "Kodi chifukwa chiyani munatitulutsa mu Eguputo kuti mudzatiphe ife, ana athu ndo zifuyo zathu ndi ludzu?"
4-Ndipo Mose anafuwulira kwa AMBUYE, nati, "Ndivachitenji ine anthuva? Pakuti atsala pang'ono kundigenda.

-Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli anapitilizabe kudandawula?
-Chifukwa chakuti analibe madzi.

-Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli analibe madzi?
-Chifukwa chakuti anali mchipululu.
-Chifukwa chakuti mchipululu muja munalibe madzi.



12-Ndakumva kudandawula kwa a Isirayeli. Ulankhule nawo ndipo wawuze kuti, "Madzulo adya nyama , ndipo m'mava adzakhuta mkate, ndipo adzadziva kuti Ine AMBUYE ndi Mulungu wanu."

-Mulungu anamuwuza Mose kuti Iye avapatsa a Isirayeli chakudya.

-Ngakhale kuti a Isirayeli samkamukhulupilira Mulungu, Mulungu anati kuti Iye avapatsa chakudya.

-Mulungu amkavathandiza a Isilayeli ngakhale kuti iwowo samkamukhulupilira Iye.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu amava thandiza anthu ngakhale kuti anthuwo sakumukhulupilira Iye.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anavalenga anthu onse.
-Chifukwa chakuti Mulungu amavakonda anthu onse.
-Chifukwa chakuti Mulungu amafuna kwapulumutsa anthu onse.
-Chifukwa chakuti Mulungu amafuna kuti anthu onse adzimukhulupilira Iye.

-Ngati sitikukhulupilira mwa Mulungu, Kodi Iye adzatipulumutsa ife?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anavasiya a Isirayeli kuti afe ndi njala?
-Kodi Mulungu anavapatsa a Isirayeli chakudya?

Tiyeni tiverenge Ekisodo 16:13a

13-Madzulo zimziri zinabwera ndi kukuta pa malo ponse pamene anamanga masakasa awo.

-Kodi Mulungu anavapatsa  Isirayeli nyama yotani madzulo akewo?
-Madzulo akewo, Mulungu anavatumizira zimziri a Isirayeli.

-Kunali zimziri zambiri mwakuti zinakuta pa malo ponse pamene anamanga masakasa awo a Isirayeli.

-Kum'mava kwake, Mulungu anavapatsanso a Isirayeli zakudya.

Tiyeni tiverenge Ekisodo 16:13b-15 ndi 31a

13-Ndipo ku m'mva kwake kunali mame pa bwalo lonse lozungulira masakasa awowo.
14-Pamene anachoka mamewo, panatsala zinthu zina zoyera, zonyata, zowoneka ngati gaga, pa mchenga wa mchipululu muja.
15-Ndipo a Isirayeli ataziwona zinthu zimenezo sanazidzive, ndipo anayamba kufunsana kuti, "Kodi zinthu zimenezi ndi zichiyani? Ndipo Mose anavawuza kuti, Chimenechi ndi chakudya chimene apereka AMBUYE kuti mudzidya."
31-Anthu a Isirayeli anazipatsa dzina lakuti mana. Anali oyera ngati zipatso za mpasa ndipo ankakoma ngati timitanda tosakaniza ndi uchi.

-Kodi Mulungu anavapatsa a Isirayeli chakudya chotani kum'mava kwake?
-Mulungu anavapatsa a Isirayeli mikate.

-Mikateyo yinali paliponse kuzungulira pa masakasawo.

-Kodi ana a Isirayeli anayitcha dzina lakuti chiyani mikate imene anapereka Mulungu ija?



-Mana.

-Kum'mava kulikonse Mulungu amkatumiza mikate kuchokera kumwamba  kuti a Isirayeli adzidya.

-Mana amene Mulungu amkavatumizira a Isirayeli kuchokera kumwamba tsiku  lililonse m'mava, chinali chidzivitso cha ubwino mtima wa Mulungu.

-Ngakhale kuti Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu, Mulungu chifukwa cha ubwino wake wa mtima analonjeza zotumiza Mpulumutsi kuti adzvapulumutse anthu onse.

-Ngakhale kuti Nowa ndi banja lake anali ochimwa, Mulungu chifukwa cha ubwino wake wa mtima anavateteza iwowo ku chigumula cha madzi.

-Ngakhale kuti a Isirayeli samkamukhulupilira Mulungu, Mulungu chifukwa cha ubwino wake wa mtima, anavapulumutsa iwo ku ukapolo wa ku Eguputo.

-Ngakhale kuti a Isirayeli samkakhulupilira kuti Mulungu mpaka avapulumutse iwo, Mulungu chifukwa cha ubwino wake wa mtima, anayigava Nyanja Yofiira kuti iwowo amuthave Farawo ndi asilikali ake.

-Zonsezi ndi zidzivitso za ubwino mtima wa Mulungu.

-Mu zaka zonse zimene a Isirayeli anali mchipululu, Mulungu ankavapatsa mana tsiku lililonse.

Tiyeni tiverenge Ekisodo 16:35

35-A Isirayeli anadya mana kwa zaka 40, mpaka pamene anafika ku malire a dziko la Kanani kumene anakakhala.